Apa ndiye kuti msonkho mudzalipira pa phindu lomwe ndi MK2,000,000 motere:

- **K1,200, 000 yoyambilira msonkho wake ndi 0% (kapena palibe msonkho)**
- **K800, 000 ndi yomwe yatsala**
- **Msonkho wa pandalama yokwana K800, 000 udulidwa pa 30% yomwe ndi K240, 000**
- **Msonkho wonse ndi: = K240, 000**

Apa zikusonyeza kuti msonkho womwe munthu apereke mchakachi potengera phindu lonse wapanga la K2, 000,000 ndi K240, 000.

Nkofunika kuti muzisunga ndondomeko yanu yomwe ikuonetsa zinthu zokhazo zogwirizana ndi pa bizinesi yanu osati zinthu zina monga kugula nsapato ya mwana wanu. Izi sizikugwirizana ndi ndondomeko yanu ya bizinesi.

Chaka cha bizinesi yanu mumakonza nokha. Mungathe kunena kuti chaka chanu chiziyamba pa 1 January ndipo chizitha pa 31 December kapena 1 April mpaka pa 31 March chaka chotsatiracho kapenanso kuyambira pa 1 July nkuzatseka pa 30 June.

Produced by Corporate Affairs Division - MRA

Malawi Revenue Authority
Msonkho House
Independence Drive
Private Bag 247
Blantyre

Tel: +265 - 1 822 588
Fax: +265 - 1 822 302
E-mail: mrahq@mra.mw
Web: www.mra.mw

Connect with us

Develop Malawi, Pay Taxes

Kulembetsa Bizinesi mkaundula wa Msonkho

NDONDOMEKO YOYENERA POLEMBETSA BIZINESI MKAUNDULA WA MSONKHO

July 2020- June 2021

Kulembetsa bizinesi mukaundula wa Msonkho

Bungwe la MRA liri ndi maofesi ake mdziko lonse la Malawi ndipo cholinga chake ndi kutumikira inu.

Munthu aliyense amene amapanga Bizinesi ayenera kulembetsa Msonkho. Munthu ayenera kulembetsa Msonkho ngakhale Bizinesiyo ili kumudzi kapena mtauni, ngakhalenso ndiyaikulu kapena yaing'ono.

Bungwe la MRA liri ndi maofesi ake mdziko lonse la Malawi ndipo cholinga chake ndi kutumikira inu. Kulembetsa Msonkho ndi kwa ulele. Ngati mwalembetsa Msonkho a MRA adzakupatsani nambala yomwe imatchedwa Taxpayer Identication number (TPIN) kuti mudzigwiritsa ntchito polumikizana ndi Bungweli pa nkhani ya Misonkho.

Kodi ubwino wolembetsa Msonkho ndiotani?

Ubwino wolembetsa msonkho ndi wakuti:

- Anthu ena azakukhulupirirani ndipo angathe kuchita nanu bizinesi chifukwa mwaonetsa kuti ndinu mzika yodalirika.
- Inunso muzakhala ndi mwayi wopanga bizinesi mopanda mantha kuwopa a MRA.
- Mukamasunga ndondomeko ya bizinesi moyenera komanso mukamapereka msonkho wanu mokhulupirika, bungwe la MRA lidzakupatsani satifiketi yomwe imatchedwa Tax Clearance Certificate. Ndi satifiketi imeneyo mutha kupikisana ndi a bizinesi anzanu kuti mupeze kontilakiti ndi Boma kapena mabungwe a Boma.
- Certificate. Ndi satifiketi imeneyo mutha kupikisana ndi a bizinesi anzanu kuti mupeze kontilakiti ndi Boma kapena mabungwe a Boma.

Kodi munthu ukalembetsa Msonkho uyenera kutani?

Munthu ukalembetsa msonkho uyenera kusunga ndondomeko ya bizinesi. Ndondomeko ya bizinesi ndi tsatanetsatane wa momwe bizinesi yanu ikuyendera. Kaundulayu amasonyezanso ndalama zimene mwagwiritsa ntchito pogulira zinthu kapena zipangizo pa bizinesi yanu.

Tsatanetsataneyunso amawonetsa zomwe mwagulitsa kapena kulandira kuchokera mu bizinesi yanu. Choncho munthu ayenera kusunga malisiti a zomwe akugula kapena kugulitsa.

Zonse zomwe akugula aike mbali imodzi ndipo zomwe akugulitsa ayikenso pamodzi. Mwachitsanzo, ngati ndalama zomwe mwalowetsa pa bizinesi yanu ndi MK3,000,000 ndipo pokutha pa chaka mwapeza MK5,000,000, ndiye kuti phindu lanu ndi MK2,000,000.